# Maphunziro a m'Baibulo

Bible studies

# Kubadwa kwa Ambuye Yesu

1. Aneneratu za kubadwa kwa Yohane
2. Aneneratu za kubadwa kwa Yesu
3. Kubadwa kwa Yesu Kristu
4. Abusa a ku Betelehemu
5. Za Simeoni ndi za Anna
6. Anzeru a kum'mawa
7. Aphedwa ana m'Betelehemu

# 1. Aneneratu za kubadwa kwa Yohane


**Luka 1.5-25**
5. Masiku a Herode, mfumu ya Yudeya, kunali munthu wansembe, dzina lace Zakariya, wa gulu la ansembe la Abiya; ndi mkazi wace wa ana akazi a pfuko la Aroni, dzina lace Elisabeti.
6. Ndipo onse awiri anali olungama mtima pamaso pa Mulungu, namayendabe m'malamulo onse ndi zoikika za Ambuye osacimwa.
7. Ndipo analibe mwana, popeza Elisabeti anali wouma, ndipo onse awiri anakalamba.
8. Ndipo panali, pakucita iye nchito yakupereka nsembe m'dongosolo la gulu lace, pamaso pa Mulungu, monga mwa macitidwe a kupereka nsembe.
9. adamgwera maere akufukiza zonunkhira polowa iye m'Kacisi wa Ambuye.
10. Ndipo khamu lonse la anthu linalikupemphera kunja nthawi ya zonunkhira.
11. Ndipo anamuonekera iye mngelo wa Ambuye, naimirira ku dzanja lamanje la guwa la nsembe la zonunkhira.
12. Ndipo Zakariya anadabwa pamene anamuona, ndipo mantha anamgwira.
13. Koma mngelo anati kwa iye, Usaope Zakariye, cifukwa kuti lamveka pemphero lako, ndipo mkazi wako adzakubalira mwana wamwamuna, ndipo udzamucha dzina lace Yohane.
14. Ndipo udzakhala nako kukondwera ndi msangalalo ndipo anthu ambiri adzakondwera pa kubadwa kwace.
15. pakuti iye adzakhala wamkuru pamaso pa Ambuye, ndipo sadzamva konse vinyo kapena kacasu; nadzadzazidwa ndi Mzimu Woyera, kuyambira asanabadwe.
16. Ndipo iye adzatembenuzira ana a Israyeli ambiri kwa Ambuye Mulungu wao.
17. Ndipo adzamtsogolera Iye, ndi mzimu ndi mphamvu ya Eliya, kutembenuzira mitima ya atate kwa ana ao, ndi osamvera kuti atsate nzeru ya olungama mtima; kukonzekeratu Ambuye anthu okonzeka.
18. Ndipo Zakariya anati kwa mngelo, Ndidzadziwitsa ici ndi ciani? Pakuti ndine nkhalamba, ndipo zaka zace za mkazi wanga wacuruka.
19. Ndipo mngelo anayankha, nati wa iye, Ine ndine Gabrieli, woimirira pamaso pa Mulungu; ndipo ndinatumidwa kwa iwe kudzalankhula nawe, ndi kuuza iwe uthenga uwu wabwino.
20. Ndipo taona, udzakhala wotonthola ndi wosakhoza kulankhula, ufikira tsiku limene zidzacitika izi, popeza uti sunakhulupirira mau anga, amene adzakwanitsidwa pa nyengo yace.
21. Ndipo anthu analikulindira Zakariya, nazizwa ndi kucedwa kwace m'kacisimo.
22. Koma m'mene iye anaturukamo, sanatha kulankhula nao; ndipo anazindikira kuti iye adaona masomphenya m'Kacisimo. Ndipo iye analinkukudola iwo, nakhalabe wosalankhula.
23. Ndipo kunali, pamene masiku a utumiki wace anamarizidwa, anamuka kunyumba kwace.
24. Ndipo atatha masiku awa, Elisabeti mkazi wace anaima; nadzibisa miyezi isanu, nati,
25. Ambuye wandicitira cotero m'masiku omwe Iye anandipenyera, kucotsa manyazi anga pakati pa anthu.

**Mafunso**
1. Werengani ndime 6. Kodi ndi zinthu zabwino zotani zimene zinanenedwa za Elisabeti ndi Zakariya?
2. Kodi izo zingakambidwe pali inenso?
3. Ndi ciani cimene cinacitika mu Kacisi? Ndi m'ndime izi mwapeza yankho?
4. Kodi zinanenedwa zokhuza Yohane ndi zotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi nchito ya Yohane ndi yotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Zakariya anakhulupirira mngelo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi ndi cilango cotani cimene cinapatsidwa cifukwa ca kusakulupirira mngelo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Nanga inu mumakhulupirira zonse zimene Mulungu akuuzani?
9. Ndi cifukwa ciani cinali codabwitsa kuti Elisabeti anali ndi pathupi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Lembani mayankho pa malo ao ndipo lembani liu mogwiritsa nchito malembo ozunguluka

1. Dzina la mngelo
2. Dzina la mwana
3. Yohane akonzekeratu ........ anthu okonzeka
4. Dzina la amai
5. Zakariya anapita ku Kacisi kupereka ..........




## 2. Aneneratu za kubadwa kwa Yesu

**Luka 1.26-56**

26 Ndipo mwezi wacisanu ndi cimodzi mngelo Gabrieli anatumidwa ndi Mulungu kunka ku mudzi wa ku
Galileya dzina lace Nazarete,
27 kwa namwali wopalidwa ubwenzi ndi mwamuna, dzina lace Yosefe, wa pfuko la Davide; ndipo dzina lace
la namwaliyo ndilo Mariya.
28 Ndipo pakulowa mngelo anati kwa iye, Tikuoneni, wocitidwa cisomo, Ambuye ali ndi iwe.
29 Koma iye ananthunthumira ndi mau awa, nasinkhasinkha kulankhula uku nkutani.
30 Ndipo mngelo anati kwa iye, Usaope, Mariya; pakuti wapeza cisomo ndi Mulungu.
31 Ndipo taona, udzakhala ndi pakati, nudzabala mwana wamwamuna, nudzamucha dzina lace Yesu.
32 Iye adzakhala wamkuru, nadzachedwa Mwana wa Wamkurukuru: ndipo Ambuye Mulungu adzampatsa
iye mpando wacifumu wa Davide atate wace:
33 ndipo iye adzacita ufumu pa banja la Yakobo ku nthawi zonse; ndipo ufumu wace sudzatha.
34 Koma Mariya anati kwa mngelo, ici cidzacitika bwanji, popeza ine sindidziwa mwamuna?
35 Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkulukulu
idzakuphimba iwe: cifukwa cacenso Coyeraco cikadzabadwa, cidzachedwa Mwana wa Mulungu.
36 Ndipo taona, Elisabeti mbale wako, iyenso ali ndi pakati pa mwana wamwamuna m'ukalamba wace; ndipo
mwezi uno uli wacisanu ndi cimodzi wa iye amene ananenedwa wouma.
37 Cifukwa palibe mau amodzi akucokera kwa Mulungu adzakhala opanda mphamvu.
38 Ndipo Mariya anati, Onani, mdzakazi wa Ambuye; kukhale kwa ine monga mwa mau anu. Ndipo mngelo
anacoka kwa iye.
39 Ndipo Mariya ananyamuka masiku amenewa, namuka ndi cangu ku dziko la mapiri ku mudzi wa Yuda;
40 nalowa m'nyumba ya Zakariya, nalankhula Elisabeti.
41 Ndipo panali pamene Elisabeti anamva kulankhula kwace kwa Mariya, mwana wosabadwayo anatsalima
m'mimba mwace; ndipo Elisabeti anadzazidwa ndi Mzimu Woyera;
42 nakweza mau ndi mpfuu waukuru, nati, Wodalitsika iwe mwa akazi, ndipo codalitsika cipatso ca mimba
yako,

43 Ndipo ici cicokera kuti kudza kwa ine, kuti adze kwa ine amace wa Ambuye wanga?
44 Pakuti ona, pamene mau a kulankhula kwako analowa m'makutu anga, mwana anatsalima ndi msangalalo m'mimba mwanga.
45 Ndipo wodala ali iye amene anakhulupirira; cifukwa zidzacitidwa zinthu zimene Ambuye analankhula naye.
46 Ndipo Mariya anati, Moyo wanga ulemekeza Ambuye,
47 Ndipo mzimu wanga wakondwera mwa Mulungu Mpulumutsi wanga.
48 Cifukwa iye anayang'anira umphawi wa mdzakazi wace;
Pakuti taonani, kuyambira tsopano, anthu a mibadwo yonse adzandichula ine wodala.
49 Cifukwa iye Wamphamvuyo anandicitira ine zazikuru; Ndipo dzina lace liri loyera.
50 Ndipo cifundo cace cifikira anthu a mibadwo mibadwo Pa iwo amene amuopa iye.
51 Iye anacita zamphamvu ndi mkono wace; Iye anabalalitsa odzitama ndi mlingaliro wa mtima wao,
52 iye anatsitsa mafumu pa mipando yao yacifumu, Ndipo anakweza aumphawi,
53 Anawakhutitsa anjala ndi zinthu zabwino, Ndipo eni cuma anawacotsa opanda kanthu.
54 Anathangatira Israyeli mnyamata wace, Kuti akakumbukile cifundo,
55 (Monga analankhula kwa makolo athu) Kwa Abrahamu ndi kwa mbeu yace ku nthawi yonse.
56 Ndipo Mariya anakhala ndi iye ngati miyezi itatu, nabweranso kunyumba kwacekunyumba kwace.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la mngelo amene anapita kwa Mariya. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi mngelo anati ciani kwa Mariya? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi dzina la Mwana linayenera kukhala ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Uyu ndi Mwana wa yani kulingana ndime ya 32?
5. Kodi ndi kotheka bwanji kuti ico cinacitika? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Mariya anapita kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Elisabeti anati ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Kodi Mariya anacita ciani pamene anakomana ndi Elisabeti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
9. Kodi mumalemekeza Mulungu? Ndi cifukwa ciani mumacita tero? Nanga tingamulemekeze bwanji Mulungu?

## 3. Kubadwa kwa Yesu Kristu

**Luka 2.1-7**
1. Ndipo kunali masiku aja, kuti lamulo linaturuka kwa Kaisara Augusto kuti dziko lonse lokhalamo anthu lilembedwe;
2. ndiko kulembera koyamba pokhala Kureniyo kazembe wa Suriya.
3. Ndipo onse anamuka kulembedwa, munthu ali yense ku mudzi wace.
4. Ndipo Yosefe yemwe anakwera kucokera ku Galileya, ku mudzi wa Nazarete, kunka ku Yudeya, ku mudzi wa Davide, dzina lace Betelehemu, cifukwa iye anali wa banja ndi pfuko lace la Davide;
5. kukalembedwa iye mwini pamodzi ndi Mariya, wopalidwa naye ubwenzi; ndi uyu anali ndi pakati,
6. Ndipo panali pokhaia iwo komweko, masiku ace a kubala anakwanira.
7. Ndipo iye anabala mwana wace wamwamuna woyamba; namkulunga iye m'nsaru, namgoneka modyera ng'ombe, cifukwa kuti anasowa malo m'nyumba ya alendo.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la kaisara amene anafuna kuti dziko lonse lokhalamo anthu lilembedwe. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi cifukwa ciani Yosefe anapita ku Betelehemu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Chulani dzina la mkazi wopalidwa naye ubwenzi. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

4. Kodi Mariya anacita ciani kwa Mwana wace wamwamuna woyamba ndiye Yesu Kristu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Ambuye Yesu anabadwa kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Ndi cifukwa ciani anabadwa kumeneko? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Ambuye Yesu anabadwanso m'mtima wanu? Kodi mumamkonda ndi mtima wanu wonse?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao ndipo pezani yankho

Ndi ciani cimene calembedwa m'Mateyu 1.21?

| | | | |
|---|---|---|---|
| 25 | 5 | 19 | 21 |

| | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 16 | 1 | 11 | 21 | 20 | 9 | | 9 | 25 | 5 | 25 | 15 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 4 | 26 | 1 | 16 | 21 | 12 | 21 | 13 | 21 | 20 | 19 | 1 |

| | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 14 | 20 | 8 | 21 | | 1 | 3 | 5 | | 11 | 21 |

| | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 13 | 1 | 3 | 9 | 13 | 17 | | 1 | 15 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |
| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |
| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |

## 4. Abusa a ku Betelehemu

**Luka 2.8-20**

8. Ndipo panali abusa m'dziko lomwelo, okhala kubusa ndi kuyang'anira zoweta zao usiku.
9. Ndipo mngelo wa Ambuye anaimirira pa awo, ndi kuwala kwa Ambuye kunawaunikira kozungulira; ndipo anaopa ndi mantha akuru.
10. Ndipo mngelo anati kwa iwo, Musaope; pakuti onani, ndikuuzani inu uthenga wabwino wa cikondwero cacikuru, cimene cidzakhala kwa anthu onse;
11. pakuti wakubadwirani inu lero, m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Kristu Ambuye.
12. Ndipo ici ndi cizindikilo kwa inu: Mudzapeza mwana wakhanda wokuta ndi nsaru atagona modyera.
13. Ndipo dzidzidzi panali pamodzi ndi mngeloyo ambirimbiri a gulu la Kumwamba, natamanda Mulungu nanena,
14. Ulemerero ukhale kwa Mulungu Kumwambamwamba, Ndi mtendere pansi pano mwa anthu amene akondwera nao.


15. Ndipo panali, pamene angelo anacokera kwa iwo kunka Kumwamba, abusa anati wina ndi mnzace, Tipitiretu ku Betelehemu, tikaone cinthu ici cidacitika, cimene Ambuye anatidziwitsira ife.
16. Ndipo iwo anadza ndi cangu, napeza Mariya ndi Yosefe, ndi mwana wakhanda atagona modyera.
17. Ndipo iwo, m'mene anaona, anadziwitsa anthu za mau analankhulidwa kwa iwo a mwana uyu,
18. Ndipo anthu onse amene anamva anazizwa ndi zinthu abusa adalankhula nao.
19. Koma Mariya anasunga mau awa onse, nawalingalira mumtima mwace.
20. Ndipo abusawo anabwera, nalemekeza ndi kutamanda Mulungu pa zinthu zonse anazimva, naziona, monga kunalankhulidwa kwa iwo.

**Mafunso**

1. Ndi yani amene anaweta usiku? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi abusa anaona ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi mngelo anati ciani ku abusa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi angelo anaimba nyimbo iti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi abusa anayenda kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi abusa anacita ciani ataona Mariya, Yosefe ndi Mwana wakhanda? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi munapeza kale Yesu m'umoyo wanu?
8. Ndi cifukwa ciani kubadwa kwa Yesu ndiko uthenga wabwino?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao ndipo pezani yankho




| | |
|---|---|
| MOSE | AMBUYE |
| ANGELO | MTENDERE |
| YOSEFE | KUWALA |
| DAVIDE | MANTHA |
| ABUSA | MWANA |

# 5. Za Simeoni ndi za Anna

**Luka 2.21-38**

21. Ndipo pamene panakwanira masiku asanu ndi atatu akumdula iye, anamucha dzina lace Yesu, limene anachula mngeloyo asanalandiridwe iye m'mimba.
22. Ndipo pamene anakwanira masiku a kukonza kwao, monga mwa cilamulo ca Mose, iwo anakwera naye kunka ku Yerusalemu, kukamsonyeza iye kwa Ambuye,
23. (monga mwalembedwa m'cilamulo ca Ambuye, kuti mwamuna ali yense wotsegula pa mimba ya amace adzanenedwa wopatulika wa kwa Ambuye)
24. ndi kukapereka nsembe monga mwanenedwa m'citamulo ca Ambuye, njiwa ziwiri, kapena maunda awiri.
25. Ndipo onani, m'Yerusalemu munali munthu, dzina lace Simeoni; ndipo munthu uyu, wolungama mtima ndi wopemphera, anali kulindira matonthozedwe a Israyeli; ndipo Mzimu Woyera anali pa iye.
26. Ndipo anamuuululira Mzimu Woyera kuti sadzaona imfa, kufikira adzaona Kristu wace wa Ambuye.
27. Ndipo iye analowa kuKacisi ndi Mzimu: ndipo pamene atate ndi amace analowa ndi kamwanako Yesu, kudzamcitira iye mwambo wa cilamulo,
28. pomwepo iye anamlandira iye m'manja mwace, nalemekeza Mulungu, nati,
29. Tsopano, Ambuye, monga mwa mau anu aja,Lolani ine, kapolo wanu, ndicoke mumtendere;
30. Cifukwa maso anga adaona cipulumutso canu,
31. Cimene munakonza pamaso pa anthu onse,
32. Kuunika kukhale cibvumbulutso ca kwa anthu a mitundu, Ndi ulemerero wa anthu anu Israyeli.
33. Ndipo atate ndi amace anali kuzizwa ndi zinthu zolankhulidwa za iye
34. Ndipo Simeoni anawadalitsa, nati kwa Mariya amace, Taona, Uyu waikidwa akhale kugwa ndi kunyamuka kwa anthu ambiri mwa. Israyeli; ndipo akhale cizindikilo cakutsutsana naco;
35. eya, ndipo lupanga lidzakupyoza iwe moyo wako; kuti maganizo a m'mitima yambiri akaululidwe.
36. Ndipo panali Anna, mneneri wamkazi, mwana wa Fanueli, wa pfuko la Aseri; amene anali wokalamba ndithu, nakhala ndi mwamuna wace, kuyambira pa unamwali wace,
37. zaka zisanu ndi ziwiri, ndipo anali wamasiye wa kufikira zaka zace: makumi asanu ndi atatu mphambu zinai, amene sanacoka kuKacisi, wotumikira Mulungu ndi kusala kudya ndi kupemphera usiku ndi usana.
38. Ndipo iye anafikako pa nthawi yomweyo, nabvomerezanso kutama Mulungu, nalankhula za iye kwa anthu onse akuyembekeza ciombolo ca Yerusalemu.

**Mafunso**

1. Ndi cifukwa ciani Yosefe ndi Maria anapita ku sunagoge ku Yerusalemu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Chulani dzina la munthu wolungama ndi wopemphera. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi munthuyo analindira ciani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Mzimu Woyera adamuuza ciani kulingana ndi ndime ya 26?
5. Kodi Simeoni anati ciani pamene analandira Yesu m’manja mwake? Ndi m’ndime izi mwapeza yankho?
6. Chulani dzina la mneneri wamkazi. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi tingakhale bwanji Akristu eni-eni monga Simeoni ndi Anna?

## 6. Anzeru a kum’mawa

**Mateyu 2.1-12**


1. Ndipo pa kubadwa kwace kwa Yesu m’Betelehemu wa Yudeya m’masiku a Herode mfumu, onani, Anzeru a
kum’mawa anafika ku Yerusalemu.
2. Nati, Ali kuti amene anabadwa Mfumu ya Ayuda? Cifukwa tinaona nyenyezi yace kum’mawa, ndipo tinadzera kudzamlambira Iye.
3. Ndipo Herode mfumuyo pakumva ici anabvutika, ndi Yerusalemu yense pamodzi naye.
4. Ndipo pamene anasonkhanitsa ansembe akuru onse ndi alembi a anthu, anafunsira iwo, adzabadwira kuti Kristuyo?
5. Ndipo anamuuza iye, M’Betelehemu wa Yudeya; cifukwa kunalembedwa kotere ndi mneneri, kuti,
6. Ndipo iwe Betelehemu, dziko a Yudeya, sukhala konse wamng’onong’ono mwa akuru a Yudeya. Pakuti
Wotsogolera adzacokera mwa iwe, Amene adzaweta anthu anga Aisrayeli. 7. Pomwepo Herode anawaitana
Anzeruwo m’tseri, nafunsitsa iwo nthawi yace idaoneka nyenyeziyo.
8. Nawatumiza ku Betelehemu, nati, Yendani mufunitsitse za kamwanako; ndipo pamene mudzampeza, mundibwezere mau, kuti inenso nidzadze kudzamlambira Iye.
9. Ndipo iwo, m’mene anamva mfumu, anamuka; ndipo onani,
nyenyezi ija anaiona kum’mawa, inawatsogolera iwo, kufikira inadza niima pamwamba pomwe panali kamwanako,
10. Ndipo iwo poona nyenyeziyo, anakondwera ndi kukondwera kwakukuru.
11. Ndipo pofika ku nyumba anaona kamwanako ndi Mariya amace, ndipo anagwa pansi namgwadira Iye; namasula cuma cao, nampatsa Iye mitulo, ndiyo golidi ndi libano ndi mure.
12. Ndipo iwo, pocenjezedwa m’kulota kuti asabwerere kwa Herode, anacoka kupita ku dziko lao pa njira yina.

**Mafunso**

1. Ndi cifukwa ciani anzeru anayenda ku Yerusalemu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi anafuna kuona yani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi mfumu Herode anadziwa bwanji kuti mfumu adzabadwira ku Betelehemu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Herode anafunsa anzeru kubwerera. Ananena, ‘Ndidzadza kudzamlambira Iye’. Kodi ananena coonadi kapena bodza? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi anzeru anacita ciani pamene anafika ku nyumba ya Yesu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi anapatsa Yesu ciani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Ndi cifukwa ciani anzeru sanabwerere ku Herode? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
8. Mfumu Herode analola anzeru kupita kwa Yesu koma iye yekha sanapite. Nanga inu, munalandira kale cipulumutso cocokera kwa Yesu kapena mumalankhula cabe za Iye?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao ndipo pezani yankho




ANZERU AIGUPTO HERODE

NYENYEZI LIBANO MFUMU

YUDEYA KRISTUYO

MNENERI GOLIDI

## 7. Aphedwa ana m’Betelehemu

**Mateyu 2.13-23**

13. Ndipo pamene iwo anacoka, onani, mngelo wa Ambuye anaonekera kwa Yosefe m'kulota, nati, Tauka, nutenge kamwanako ndi amace, nuthawire ku Aigupto, nukakhale kumeneko kufikira ndidzakuuza iwe; pakuti Herode adzafuna kamwana kukaononga Iko.
14. Ndipo iye ananyamuka natenga kamwana ndi amace usiku, nacoka kupita ku Aigupto;
15. nakhalabe kumeneko kufikira atamwalira Herode; kuti cikacitidwe conenedwa ndi Ambuye mwa mneneri kuti,
16. Pamenepo Herode, poona kuti anampusitsa Anzeruwo, anapsa mtima ndithu, natumiza ena kukaononga tiana tonse ta m'Betelehemu ndi ta m'miraga yace yonse, takufikira zaka ziwiri ndi tating'ono tonse, monga mwa nthawi imeneyo iye anafunsitsa kwa Anzeruwo.
17. Pomwepo cinacitidwa conenedwa ndi Yeremiya mneneri, kuti,
18. Mau anamveka m'Rama, Maliro ndi kucema kwambiri; Rakele wolira ana ace, Wosafuna kusangalatsidwa, Cifukwa palibe iwo.
19. Koma pakumwalira Herode, onani, mngelo wa Ambuye anaonekera m'kulota kwa Yosefe m'Aigupto,
20. nati, Tauka, nutenge kamwana ndi amace, nupite ku dziko la Israyeli: cifukwa anafa uja wofuna moyo wace wa kamwanako.

21. Ndipo anauka iye, natenga kamwana ndi amace, nalowa m'dziko la Israyeli.
22. Koma pakumva iye kuti Arikelao anali mfumu ya Yudeya m'malo mwa atate wace Herode, anacita mantha kupita kumeneko; ndipo pamene anacenjezedwa ndi Mulungu m'kulota, anamuka nalowa ku dziko la Galileya,
23. nadza nakhazikika m'mudzi dzina lace Nazarete kuti cikacitidwe conenedwa ndi aneneri kuti, Adzachedwa Mnazarayo.

**Mafunso**

1. Ndi yani amene anauza Yosefe kucoka ku Aigupto? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi cifukwa ndi ciani anafunikira ku pita ku Aigupto? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Herode anacita ciani pamene anaona kuti anampusitsa anzeruwo? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Chulani dzina la mneneri amene ananena kale zonse zimene zidzacitika. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi tingaphunzire ciani m’ndime izi?

**Sewero**

Pezani mau onse

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| Q | J | O | O | T | P | U | G | I | A |
| U | R | E | Z | N | A | Z | H | N | G |
| A | F | F | X | O | R | U | E | A | E |
| N | L | S | S | L | Y | J | R | Z | L |
| A | A | H | R | E | K | X | O | A | E |
| W | W | A | T | G | T | R | D | R | K |
| M | M | A | V | N | X | U | E | E | A |
| A | M | U | J | M | R | B | Z | T | R |
| M | O | Y | O | S | E | F | E | E | R |
| A | Y | I | M | E | R | E | Y | P | Z |

MATEYU
MNGELO
YOSEFE
AIGUPTO
HERODE
MWANA
ANZERU
RAMA
RAKELE
YEREMIYA
NAZARETE

## Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo Macitidwe a Atumwi 4.12